**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE**

*Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo*

# M'MENE MABOMA ANGAKONZEKELERE EL NIÑO WAMPHAMVU

*Kukonzekera El nino yemwe akuyembekezereka nyengo ya dzinja ya 2026/27*

*15 July 2026*

---

## 1. Mawu Oyambilira

Kauniuni wa za nyengo akusonyeza kuti El nino wa mphamvu wayamba kale kuoneka mu Nyanja ya mchere ya Pacific, ndipo chiopsezo cha El Niño chikuyembekezeka kupitirira mpaka chaka cha mawa cha 2027. Mabungwe olosera za nyengo padziko lonse lapansi akuyerekeza kuti pali kuthekera koposera 80% kuti El Niño wa mphamvu kwambiri achitika. Kuyelekeza ndi mbuyomu, zikusonyeza kuti pali kuthekera ndi 24% kuti El Niño yemwe achitike chaka chino aposa El Nino wa chaka cha 2015/16, yemwe ndi El nino wa mphamvu kwambiri kuchitika kuyambira chaka cha 1982.

Lipotili likuphatikiza upangiri wa madera osiyanasiyana operekedwa ndi Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo wa maboma onse 28 a dziko la Malawi, kuwaphatikiza m'magulu a ziopsezo, kuti zithandizire kukonzekera ntchito zosiyanasiyana mdziko lonse komanso m'maboma. Lipoti la boma lililonse laperekedwa mu chigawo cha zowonjezera(Appendix).

## 2. Chidule Cha Chiopsezo Cha El Nino Ku Dziko

Zotsatira za El Niño wamphamvu zimasiyana kwambiri malinga ndi madera. Madera a Chigawo cha Kumpoto nthawi zambiri amakhala ndi chiopsezo chochepa, ndipo chiopsezo cha ng'amba ndi mvula yambiri chimakhala chochepa komanso chiopsezo cha chilala chimakhala chochepa mpaka chapakatikati.

Madera a Chigawo cha Pakati ali ndi chiopsezo chosiyanasiyana cha nyengo ya ng'amba komanso chilala chapakatikati, pomwe chiopsezo cha mvula yambiri chimakwera m'maboma ngati Ntchisi ndi Dowa.

Chigawo cha Kumwera chili ndi chiopsezo chachikulu komanso chophatikizana: maboma khumi ndi awiri amakumana ndi nyengo ya ng'amba yapakatikati, Chilala champhamvu, komanso chiopsezo cha mvula yambiri nthawi imodzi, zomwe zikutanthauza kuti njira zothanirana ndi chilala komanso kusefukira kwa madzi ziyenera kukonzedwa zonse.

## 3. Magawo A Ziopsezo

Maboma agawidwa m'magulu asanu kutengera kuphatikiza kwa chiopsezo cha ng'amba, chiopsezo cha chilala, ndi chiopsezo cha mvula yambiri chomwe chafotokozedwa mu upangiri wa madera:

| Gawo la Chiwopsezo | Maboma(Madera) | Zomwe Zingachitike Komanso Malangizo |
|---|---|---|
| **Gawo 1 - Chiwopsezo Chochepa** | Chitipa , Karonga, Rumphi , Mzimba, Likoma (5) | Chiwopsezo chochepa cha chilala, ng'amba kapena mvula yambiri. Kukonzekera koyenera kusunga madzi okwanira. |
| **Gawo 2 — Chiwopsezo Chochepa Mpaka Chapakati** | Nkhata Bay (1) | Chiwopsezo chochepa cha ng'amba, koma chilala chochepa chingathe kuchitika; kukonzekera kuchepa kwa chinyontho(chinyezi) kukulimbikitsidwa. |
| **Gawo 3 - Chiwopsezo Chapakati** | Nkhotakota , Kasungu, Mchinji , Lilongwe, Salima, Ntchisi , Dowa, Dedza (8) | Ng'amba ya pakati komanso chilala chapakati makamaka miyezi ya JFM, ndi chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri(chiopsezo chachikulu kwambiri ku Ntchisi ndi Dowa). Imafuna kusunga chinyezi ndi kuyang'anira kusefukira kwa madzi m'deralo. |
| **Gawo 4 — Chiwopsezo Chachikulu** | Machinga, Zomba (2) | Ng'amba ya pakati komanso chilala champhamvu; chiopsezo cha mvula yambirir ndi chochepa ku Machinga koma chapakati ku Zomba. Kukonzekera chilala kuyenera kukhala patsogolo. |
| **Gawo 5 — Chiwopsezo Choopsa (Chiwopsezo Chophatikizana)** | Ntcheu, Mangochi, Balaka, Neno, Mwanza, Blantyre, Phalombe, Mulanje, Thyolo, Chiradzulu , Chikwawa, Nsanje (12) | Ng'amba ya pakati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula yambiri. Maboma 12 awa ali pa chiopsezo chachikulu ndipo pafunika kukonzekera bwino za chilala ndi kusefukira kwa madzi. |

## 4. Malangizo ndi Zina Zoyenera Kuchita

- Madera a Gawo 1-2 (Chigawo cha Kumpoto): kudziwitsa ndi kulimbikitsa anthu kutsatira njira zosunga madzi; ndi kupitiriza kuyang'anira nthawi zonse momwe mvula imayambira komanso momwe imagwera
- Madera a Gawo 3 (Chigawo cha Pakati): ayenera kuika patsogolo njira zosungira chinyezi ndi njira zaulimi zomwe zingathandize kupirira nyengo; madera omwe ali ndi chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri ( Ntchisi , Dowa, Dedza) ayeneranso kulimbikitsa kuyang'anira kusefukira kwa madzi m'deralo.
- Madera a Tier 4 (Machinga, Zomba): akuyenera kuyika patsogolo njira zochepetsa chilala ndi kusunga madzi, komanso kulimbikitsa ndi kudziwitsa anthu za chiopsezo cha kusefukira kwa madzi ku Zomba.
- Madera a Tier 5 (Chigawo cha Kumwera ): kukhazikitsa mapulani othandiza pa nkhani ya chilala ndi kusefukira kwa madzi; kukhazikitsa zipangizo zaulimi ndi kulimbikitsa ntchito zothandiza

kusunga chinyezi nyengo ya chilimwe; komanso kukhazikitsa njira zochenjeza msanga za mvula yambiri ndi kusefukira kwa madzi.

- **Maboma  onse ayenera kupitiliza kugwiritsa ntchito ulosi wa nyengo ya dzinja, pamene pali kuthekera kwakukulu ndi 80% kwa El Niño wamphamvu kwambiri.**

## 5. Zowonjezera 1: Malangizo Maboma (Madera) Onse


Table ili m'munsimu likuwonetsanso malangizo a madera onse m'dziko muno (Maboma 28 onse):


| Boma (Dera) | Malangizo a Dera |
|---|---|
| **Chitipa** | Chiwopsezo chochepa cha chilala ndi ng'amba kapena mvula yambiri panthawi ya El Niño. Madera ayenera kukonzekera njira zosungira madzi. |
| **Karonga** | Chiwopsezo chochepa cha chilala ndi ng'amba kapena mvula yambiri panthawi ya El Niño. Madera ayenera kukonzekera njira zosungira madzi. |
| **Rumphi** | Chiwopsezo chochepa cha chilala ndi ng'amba kapena mvula yambiri panthawi ya El Niño. Madera ayenera kukonzekera njira zosungira madzi. |
| **Mzimba** | Chiwopsezo chochepa cha chilala ndi ng'amba kapena mvula yambiri panthawi ya El Niño. Madera ayenera kukonzekera njira zosungira madzi komanso kupitiriza kuyang'anira nthawi zonse momwe mvula imayambira komanso momwe imagwera |
| **Nkhata Bay** | Chiwopsezo chochepa cha ng'amba; Chiwopsezo chapakatikati cha chilala. Madera ayenera kukonzekera njira zosungira chinyezi ndikulimbikitsa njira zosungira madzi. |
| **Likoma** | Chiwopsezo chochepa cha chilala ndi ng'amba kapena mvula yambiri.<br>Kupitiliza kuyang'anira kupezeka kwa madzi ndikofunikira. |
| **Nkhotakota** | Chiwopsezo chochepa cha ng'amba nthawi ya OND koma chiwopsezo chapakatikati cha ng'amba nthawi ya JFM, komanso chilala chapakatikati. Zingakhudze kukula kwa mbewu ndi kupezeka kwa madzi, zomwe zimafuna kukonzekera msanga komanso kusunga madzi. |
| **Kasungu** | Chiwopsezo chapakatikati cha ng'amba nthawi ya JFM, komanso chilala chapakatikati. Alimi ayenera kuganizira njira zosungira chinyezi komanso njira zaulimi zomwe zingathandize kupirira nyengo. |
| **Mchinji** | Chiwopsezo cha nyengo ya Ng'amba yapakatikati mpaka kufika nthawi ya JFM, chilala chochepa, komanso chiopsezo chochepa cha mvula yambiri panthawi ya JFM. Konzekerani kuti mvula sikhala ikugwa yodalirika komanso ya mphamvu nthawi zina m'madera ena. |
| **Lilongwe** | Chiwopsezo cha nyengo ya ng'amba komanso chilala cha mlingo wapakatikati koma chiopsezo chochepa cha mvula yambiri panthawi ya JFM.<br>Kusunga madzi ndi kuyang'anira machenjezo achangu a zanyengo ndikofunikira pa ulimi. |
| **Ntchisi** | Chiwopsezo cha nyengo ya ng'amba komanso chilala cha mlingo wapakatikati mpaka komanso chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri panthawi ya JFM.<br>Konzekerani mavuto akusowa kwa chinyezi komanso mvula yambiri yomwe ingawononge. |


| Boma (Dera) | Malangizo a Dera |
|---|---|
| **Dowa** | Chiwopsezo cha nyengo ya ng'amba komanso chilala cha mlingo wapakatikati mpaka komanso chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri panthawi ya JFM.<br>Konzekerani ndi kuthana ndi mavuto a kusowa kwa madzi m'minda komanso kusefukira kwa madzi m'dera. |
| **Salima** | Chiwopsezo cha nyengo ya ng'amba komanso chilala cha mlingo wapakatikati koma chiopsezo chochepa cha mvula yambiri panthawi ya JFM.<br>Kuyang'anira madzi ndi upangiri waulimi ndikofunikira. |
| **Dedza** | Ng'amba yapakatikati, chilala chapakatikati, komanso chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri. Konzekerani kusinthasintha kwa mvula, kuphatikizapo kuchepa kwa chinyontho ku mbewu, komanso mvula yambiri. |
| **Ntcheu** | Ng'amba yapakatikati, chilala chapakatikati, komanso chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri pa nthawi ya JFM.<br>Izi zikhoza kukhudza kwambiri ntchito za ulimi ndi madzi; kukonzekera bwino kukufunika. |
| **Mangochi** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula yambiri. Konzekerani mavuto akuluakulu azaulimi pamodzi ndi mavuto omwe angabwere chifukwa cha mvula yambiri. |
| **Machinga** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chochepa cha mvula yambiri pa nthawi ya JFM. Chofunika kwambiri ndi kukonzekera chilala komanso kusunga madzi. |
| **Balaka** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula. Konzekerani kuthana ndi mavuto aakulu pa ulimi wa mbewu, kupezeka kwa madzi, ndi zoopsa zokhudzana ndi nyengo ya mvula. |
| **Neno** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula. Kukonzekera bwino ng'amba yomwe ingachitike kwa nthawi yayitali komanso kuwonongeka kwa katundu ndi Ngozi chifukwa cha mvula. |
| **Mwanza** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula. Gwiritsani ntchito njira zochepetsera ng'amba ndi chilala komanso kulimbikitsa ma uthenga ndi machenjezo a zanyengo |
| **Blantyre** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula. Konzekerani kuthana ndi mavuto omwe angabwere chifukwa cha kuchepa kwa madzi komanso mavuto okhudzana ndi mvula. |
| **Zomba** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo cha mvula yambiri panthawi ya JFM. Yang'anani kwambiri pa zotsatira za chilala ndi ng'amba komanso kusefukira kwa madzi. |
| **Phalombe** | Ng'amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiopsezo chachikulu cha mvula panthawi ya JFM. Konzekerani kuchepa kwa mvula komanso mvula yambiri yomwe ingagwe. |

| Boma (Dera) | Malangizo a Dera |
|---|---|
| **Mulanje** | Ng’amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiopsezo chachikulu cha mvula panthawi ya JFM.<br>Kukhazikitsa njira zokhakika zokonzekera chilala ndi kusefukira kwa madzi. |
| **Thyolo** | Chiopsezo cha Ng’amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula yambiri. Njira zoyendetsera ulimi ndi madzi ndizofunikira kwambiri pa nyengo ya El Niño. |
| **Chiradzulu** | Chiopsezo cha Ng’amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiwopsezo chachikulu cha mvula. Konzekerani mavuto okhudzana ndi chinyezi cha mbewu komanso mvula yamphamvu. |
| **Chikwawa** | Chiopsezo cha Ng’amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiopsezo chachikulu cha mvula panthawi ya JFM. Yang'anani kwambiri pa kusowa kwa madzi, kuuma kwa mbewu, komanso mvula yomwe ingagwe yambiri. |
| **Nsanje** | Chiopsezo cha Ng’amba ya pakatikati, chilala champhamvu, komanso chiopsezo chachikulu cha mvula yambiri panthawi ya JFM. Limbikitsani kukonzekera ng’amba ndi chilala komanso kukhala tcheru ku chiopsezo cha mvula yambiri. |

## 6. Zowonjezera 2: Ziopsezo Zokhudzana ndi El Nino wa Mphamvu Ku Malawi




Extreme Rainfall Risk - JFM Season
0 - No threat
1 - Moderate
2 - Severe
3 - Extreme
Dry Spell Risk - JFM Season
0 - No threat
1 - Moderate
2 - Severe
3 - Extreme
Drought Risk
0 - No threat
1 - Moderate
2 - Severe
3 - Extreme